**EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA**

**JUNIOR SECONDARY SCHOOL LEAVING EXAMINATION (GRADE 9) – 2014**

# CINYANJA 302/2

## PEPALA LACIWIRI

## (SPECIMEN)

**(INTERNAL AND EXTERNAL CANDIDATES)**

**NTHAWI: MAOLA AWIRI** **MAKISI: 60**

**DZINA LAKO:** ______________________

**NAMBALA YAKO YA MAYESO:** ______________________

**SUKULU/DERA:** ______________________

**Cell phones are not allowed in the examination room.**
**Malamya (foni) ndi yosaloledwa m'cipinda colemberamo mayeso.**

**MALANGIZO**

Lembani mayankho anu onse m'pepala la mayeso limeneli m'malo amene aperekedwa.

| **CIGAWO** | **MAKISI OPEREKEDWA** | **MAKISI APEZEDWA** |
|---|---|---|
| **COYAMBA** | 15 | |
| **CACIWIRI** | 15 | |
| **CACITATU** | 10 | |
| **CACINAI** | 10 | |
| **CACISANU** | 10 | |
| **MAKISI ONSE** | **60** | |

**CIGAWO COYAMBA [15 MAKISI]**

**MVETSO:**

**Malangizo:** Werengani nkhani yotsatirayi mokhazikira ndiponso mosamala. Mukatero, muyankhe mafunso otsatira.

## UCIMASO MASO UNAPASULA THEMBA PA UKWATI

Mumzinda wina wochedwa Nderere, munali mtsikana wina wochedwa Themba. Mtsikanayu anali othamanga zedi ndipo maonekedwe ake anali ocititsa kaso. Maso ake anali kuoneka ngati anathiramo mkaka wa ng'ombe. Anali wamtali ndipo woyera bwino, kuyera kuja kocita kudzipanga ndi mafuta. Indedi! Anali kuti akaimirira potero, ai ndithu amuna anali 'kufa chipoyo'.

Cinali cocititsa manyazi poona kuti mtsikana wokongola cotere, anakwatiwa kwa mnyamata wofatsa ndi waulemu bwino. Anthu ambiri analephera kutsimikiza kuti mtsikanayo analidi mkazi wake wakunyumba. Khalidwe la mtsikana linali khalidwe loipitsitsa cifukwa analibe ulemu ndi anthu ndipo mwamuna wake, sanamuyese ngati munthu. Ceni-ceni cosalemekezera mwamuna wace, nkuti akulu anchito ya mkampani yaikulu mumzindawo anali atamuimitsa nchito. Paja akulu amati, 'pafupi ndi apo wafika', mtsikanayo anayamba kusokoneza maukwati ya eni, a nyumba zoyandikana nazo.

Cinatengera anthu adera kudzauza amuna a mkaziyo zomwe anali kucita. Sanabvomere ndi pang'ono ponse kuti anali kuzicitadi. Kukaca m'mawa, anali kungoti buli! Wabulika mwana wamchembere, komwe anali kupita, anali kudziwako yekha. Anthu ena maka-maka omwe anali nawo mkomboni imodzi anali kumuona Themba ndi zocitika zake.

Pakuopa kuculutsa gaga mdiwa, wina wa iwo anthu atawaona tsiku lina, anathamanga kukaitana amuna a Themba kuti akadzionere okha maso mphenya. Bamboyo anampezadi Themba ali pa ka hotera kena kodziwika bwino, ali ndi kamdala kena kosadziwika bwino mcipinda cina. Apo nkuti, anali atauza mwamuna wake kuti anaiwala kugulako mkate wa m'mawa mwake. Nthawi inali folo koloko yam'madzulo.

Cifukwa ca phokoso yomwe mwamuna wake anacita, anthu anadzala pa hotera paja ndipo ena anayamba kukuwa hule iyo! Mwacisoni ka mkazi ka kamdala kaja kanabwera ndipo kanadabwa ndi zomwe mwamuna wake anali kucita. Mwamuna wa Themba nayenso anangobwerera kunyumba ndikulonga katundu yense wa Themba, kutha kwa ukwati komweko. Themba anapita kwao kukakomboni kosaoneka bwino kochedwa Ndololo.

**MAFUNSO [15 MAKISI]**

**(i) Tsopano yankhani mafunso awa polemba lembo limene liri ndi yankho loyenera mkati mwakabokosi mwapatsidwako. [5 MAKISI]**

**1** Kodi mtsikana othamanga uja amakhala m'mzinda wanji?

- **A** Hotera
- **B** Komboni
- **C** Nderere
- **D** Ndolola

[1]

**2** Kodi cifukwa ceni-ceni comwe mtsikanayo anali kucitira ucimaso-maso cinali ciani?

- **A** Anacita kumuuza kuti acite tero
- **B** Anafuna kulanda amuna wa eni
- **C** Anafuna kupsyetsa mtima anthu
- **D** Panyumba panasowa ndalama

[1]

**3** Kodi ndani anauza amuna ake Themba zocita zake.

- **A** Anthu ena
- **B** Anzake a mwamuna wa Themba
- **C** Atate ake
- **D** Mkazi wa kamdala kaja

[1]

**4** Kodi ndi bodza lotani lomwe Themba anauza mwamuna wake kuti akakumane ndi kamdala ku Hotera?

- A Anati anakagula sopo
- **B** Anati anaiwala ndiwo kumsika
- **C** Anati anakagula nyama
- **D** Anati anakagula mkate

[1]

**5** Kodi mapeto ake a ukwati wao anali wotani?

- **A** Anthu anamenya Themba
- **B** Kamdala kaja kanathawa
- **C** Themba anakhala pa nyumba
- **D** Themba anapitikitsidwa

[1]



specimen

**(ii) Tsopano yankhani mafunso otsatirawa mofotokoza bwino. [5 MAKISI]**

6 Kodi maonekedwe a Themba anali wotani?
***Yankho:*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

7 Kodi mwamuna wa Themba anali ndi khalidwe lotani?
***Yankho:*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

8 Ncifukwa nciani anthu analephera kutsimikiza kuti Themba analidi mkazi wa mwamuna uja?
***Yankho:*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

9 Kodi Themba akabulika pabwalo, amapita kuti?
***Yankho:*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

10 Ataona kuti Themba anali ndi mwamuna wina ku Hotera kuja, mwamuna wake anacita ciani?
***Yankho:*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

**(ii) MATANTHAUZO A MAU – [5 MAKISI]**

Pezani mau omwe agwiritsidwa nchito m'nkhani mwawerenga iyi ofanana matanthauzo ndi zimene mwafunsidwa. Lembani liu limodzi cabe.

1 Themba anali mtsikana othamanga, liu iyi litanthauzanji?

***Yankho*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]

2 Amuna akaona Themba anali 'kufa chipoyo'. Kodi ici citanthauzanji?

***Yankho*** ____________________________________________

____________________________________________ [1]



Specimen

3 Mwambi woti 'pafupi ndi apo wafika' utanthauzanji?

***Yankho*** ________________________________________

________________________________________ [1]

4 Nanga kuchulutsa gaga mdiwa ndiko kuti ciani?

***Yankho*** ________________________________________

________________________________________ [1]

5 Anthu anauza mwamuna wa Themba kuti adzionera 'maso mphenya' kodi liu iri litanthauzanji?

***Yankho*** ________________________________________

________________________________________ [1]

**CIGAWO CACIWIRI [15 MAKISI]**

**CINENEDWE**

Yankhani mafunso onse m'cigawo ici.

1 Ikani afotokozi a msinkhu m'malo oyenera.

**(a)** Pa atsikana atali atali, Tikambenji yekha anali
***Yankho:*** ________________________________________ [1]

**(b)** Ganizani analowa mu geredi loyamba akali mwana
***Yankho:*** ________________________________________ [1]

2 Limbikani ananena mau oipa.
Yambani ciganizo ndi;

Mau oipa ________________________________________ [1]

3 Pangani maina kucokera ku aneni awa:

**(i)** Langa
***Yankho:*** ________________________________________ [1]

**(ii)** Lima
***Yankho:*** ________________________________________ [1]

**(iii)** Lemba
***Yankho:*** ________________________________________ [1]

Specimen

**4** Sinthani ciganizo ciri m'munsimu pa kusonyeza kuti cinthu cinacitika kamodzi kale.

Wabwera yeka mayase.

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

**5** Sinthani ciganizo ciri m'munsimu pakusonyeza kuti cinthu cidzacitika mtsogolo.

Ana akudya nsima.

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

**6** Sinthani ciganizo ciri m'munsimu pakusonyeza kuti cinthu cidzacitika nthawi zonse.

Atsikana anabvala zobvala zabwino

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

**7.** **(a)** Kodi apamneni nciani?

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

(b) Pangani ziganizo ndi apamneni opatsidwa awa.

**(i)** Mofulumira
***Yankho:*** ______________________________________________ [1]

**(ii)** Kambiri
***Yankho:*** ______________________________________________ [1]

**8.** Sinthani ziganizo izi zomwe ziri zoyankhula mwini (direct speech) kuti zikhale ziganizo zoyankhula mopanda chindunji (indirect speech).

**(a)** "Kodi wadya nsima maliya?" agogo anafunsa

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

**(b)** "Aphunzi ambiri athawa mkalasi," aphunzitsi anadandaula.

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]

**(c)** "Bwera kuno mwana iwe!" amai anapfuula.

***Yankho*** ______________________________________________

______________________________________________ [1]



Specimen

**CIGAWO CACITATU [10 MAKISI]**

**KUMASULIRA [10 MAKISI]**

Masulirani nkhani iri m'munsimu kuti ikhale m'Cinyanja comveka bwino.

1 I write to remind you that Zambia will be 50 years old by 24th October this year.

***Yankho***

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________ [2]

2 This means that Zambia will attain 50 years of independence from colonial rule.

***Yankho***

______________________________________________

______________________________________________ [2]

3 Boys, girls and teachers are busy making preparations for the big day.

***Yankho***

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________ [2]

4 For this reason, it is important for you to attend this celebration which will take place at my school on 24th October this year.

***Yankho***

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________ [2]

5 There will be activities such as; singing, dancing, eating and sporting activities.

***Yankho***

______________________________________________ [2]

Specimen

**CIGAWO CACINAI**

**CIFUPIKITSO: [10 MAKISI]**

Lembani mfundo zikulu-zikulu zisanu kucokera mu nkhani yomwe mwawerenga mu mvetso.

Specimen

**CIGAWO CACISANU:MIYAMBI** **[10 MAKISI]**

**Yankhani mafunso onse a m'cigawo ici:**

**1** Ndi mwambi uti umene ufanana ndi uwu woti, "Mwana m'nyanja alimbikira mpani wace.

**A** Kukana nsalu ya akulu nkubviika.

**B** Lero lomwe linadetsa mnthanga.

**C** Mpani wambewa utsatira mwini.

**D** Safunsa anadya phula. [1]

**2** Kodi mwambi uwu woti, "kupulumukira m'kamwa mwa mbuzi,' utanthauzanji?

**A** Mwambi wotsutsa munthu wonena bodza.

**B** Mwambi wakuletsa kulonjezeratu cinthu cobvuta.

**C** Mwambi wotsutsa munthu amene amanenanena zakale zothaitha.

**D** Mwambi wonenedwa ngati anthu awiri atengana mlandu ndi kumatsutsana. [1]

**3** Kodi mwambi woti, "kulamula bvumbwe nkulinga uli ndi nkhuku" uthanthauzanji?

**A** Mwambi woletsa zakunama ngati munthu wina aulula za mnzake.

**B** Mwambi woponyedwa ku munthu wofulumira kunena modzitama.

**C** Mwambi wotsutsa munthu wonena bodza.

**D** Safunsa anadya phula. [1]

**4** Sankhani ndi kulemba mwambi wina umene ufanana ndi uwu woti, "cisoni cinapha msema-mitondo'.

**A** Wampota bwanji ndiri ku ula.

**B** Cisoni cinapha nkhwali.

**C** Waona nkhanga maanga wataya nkhwali.

**D** Cala siciloza mwini. [1]

**5** Lembani tanthauzo la mwambi woti, "waona nkhanga maanga wataya nkhwali".

***Yankho:***________________________________________ [1]

**6** Fotokozani tanthauzo lake la mwambi uwu. "Tsoka sasimba koma mwai".

***Yankho:***________________________________________ [1]

Specimen

**7** Tsirizani mwambi uwu: ici nciani

***Yankho:***________________________________________ [1]

**8** Fotokozani tanthauzo la mwambi woti, "umanena catsitsa dzaye poti njobvu ithyoke mnyanga"

***Yankho:***________________________________________ [1]

**9** Tsirizani mwambi uwu: kunena kwa ndithe-ndithe

***Yankho:***________________________________________ [1]

**10** Kodi mwambi woti, "pawiri sipauzirika" utanthauzanji?

***Yankho:***________________________________________ [1]

**MAYESO ANU ATHA**

Specimen